**EXAMINATIONS COUNCIL OF ZAMBIA**

**GRADE SEVEN COMPOSITE EXAMINATION – 2021**

# Cinyanja

**SUBJECT 5/1** **NTHAWI: MPHINDI 60**

**TD/NYA5/G7/2021**

1 Werengani dongosolo la macitidwe a mayeso awa mwatsatane-tsatane ndi mosamala.

2 Musatsekule tsamba iri musanauzidwe kucita tero. Aphunzitsi anu adzakuuzani nthawi yotsekulira pepalali kuti muyambe kuyankha mafunso.

3 Pepala iri liri ndi mafunso okwanira makumi asanu (50) cabe mu zigawo zisanu ndi cimodzi. Muyankhe mafunso onse. Mukatsiriza kuyankha mafunso a m'cigawo cimodzi, musayembekezere kuuzidwa kuti mupite ku cigawo cina. Pitirizani kulemba mpaka kutsiriza mafunso onse.

4 Funso lirilonse liri ndi mayankho anai (4) amene limodzi cabe ndilo loyenera lopambana ena onse. Mukasankha yankho lanu, phimbani yankho lanulo pophimba mkombero muli yankho mwasankha motere.

**CITSANZO:** [A] [B] [ ] [D]

Yankho lacitatu **'C'** ndilo lopambana onse. Conco phimbani yankho liri mu mkombero **'C'**.

Werengani malangizo ndi zitsanzo zonse ziri m'cigawo ciriconse molingalira bwino ndiponso mosamala. Musanaphimbe yankho lanu muwerenge mayankho onse mosamala.

5 Ngati mufuna kusintha yankho mwasankha poyamba, fafanizani yankho loyamba mwaukhondo pogwiritsa nchito cofafanizira copanda dothi.

6 Musataye nthawi yaitali kufuna kuyankha mafunso obvuta. Mungabwerere ku mafunsowo potsirizira pake ngati kwakhala nthawi.

7 Ngati mwatsiriza kuyankha mafunso onse, kukatsala nthawi, gwiritsani nchito mphindi zotsalirazo kupititsamo mu mayankho anu. Onani kuti mwayankha **mafunso onse. Onetsetsani kuti pa pepala lanu la mayanko pali dzina lanu, nambala ya mayeso yanu, dzina la sukulu lanu. Pa mwamba palembedwa "paper 5."**

8 Imikani manja anu tsopano ngati:

**(i)** muli ndi funso.

**(ii)** pepala lanu la mayankho siliri lolongosoka



pdfxstore.com

## CIGAWO COYAMBA

### Malangizo

Funso liri lonse liyamba ndi ciganizo comwe ciri ndi liu kapena dera lina losowa m'malo amene aonetsedwa. Munsi mwake mudzapezamo mau kapena madera a ziganizo anai. Liu limodzi mwa mau anai ndilo litsiriza bwino ciganizo conse.

**Citsanzo:** Mnyamata aliyense ali ndi kakhasu ... kobzalira mtedza.

- **A** kanga
- **B** langa
- **C** kake
- **D** yake

Yankho **"C"** kake, ndilo liu litsiriza bwino ciganizo conse. Conco munakaphimba yankho **"C"** mu mkombero motere:

[A] [B] [ ] [D]

**Tsopano yankhani mafunso otsatira:**

**1** Nkhwanga inagwera munsi ... mtengo.

- **A** ku
- **B** mwa
- **C** pa
- **D** wa

**2** Maiwase anayankha funso ...

- **A** mogona.
- **B** mothawa.
- **C** mwaluso.
- **D** mwanzeru.

**3** Abusa amapita ... Chalichi pa sabata.

- **A** mu
- **B** ku
- **C** pa
- **D** kwa

**4** Amake Belita akhala ... mphasa.

- **A** ku
- **B** mu
- **C** ndi
- **D** pa

5 ... udzapita kuti lero?

A Awo
B Ife
C Mu
D Iwe

6 Gulu ... linapambana pa masewera a mpira pa cikho ca dziko lonse lapansi ndi la France.

A kumene
B limene
C pamene
D yamene

7 A za ulimi ali yakali-yakali m'midizi kuphunzitsa alimi za ... a cinangwa.

A madulidwe
B magaulidwe
C malimidwe
D mapalidwe

8 Atate ... galimoto la kunchito.

A apalasa
B athamanga
C aulutsa
D ayendetsa

9 Nkhokwe ... ya a Maiwase yapsya.

A kadothi
B kakakulu
C yaikulu
D zazikulu

10 Kamwana kaja. . .gona kale.

A ka
B ta
C twa
D za

11 Cimtengo ... cija cinagwa dzulo.

A cacitali
B kakafupi
C twatutali
D zazitali

12 Yakobo anakondwera kwambiri ... anaonana ndi Maliko.

A ngakhale
B m'mene
C pamene
D yemwe

13 Mwana wa ngo'mbe amachedwa kuti ...

A kabulu.
B kamwana.
C kang'ombe.
D litole.

14 ... ! Ndizo wacita izi?

A Uaa
B Uee
C Uoo
D Uuu

15 Mtedza ... atate analima watha munkhokwe.

A cimene
B umene
C wamene
D zimene

**CIGAWO CACIWIRI**

Cigawo ici ciri ndi mbali ziwiri .Mbali yoyamba iri ndi ziganizo zimene ziri **m'cindunji ndi m'cisandunji** (direct and indirect speech). Mbali yaciwiri iri ndi mafunso pa zopumira. Yankhani mafunso kulingana ndi malangizo opezeka pa mbali iri yonse.

**Cindunji ndi cisandunji** (direct and indirect speech) sankhani ziganizo zimene zalembedwa moyenera mwaziganizo zopezeka pa mafunso **16** ndi **17.**

16 Sankhani ciganizo coyenera mwa ziganizo zinaizi.

A Fashon Sakala anati, "Ndisewera bwino mpira makono."
B "Fashon sakala anali kuti, "ndisewera bwino mpira makono.
C Fashon Sakala ananena kuti," asewera bwino mpira makono."
D "Fashon sakala ananena kuti, "asewera bwino mpira makono.

17 Sankhani ciganizo coyenera mwa ziganizo zinaizi.

A Yosefe anacita bwino pa mayeso ake a giredi 7 caka catha.
B Yosefe anacita munshe pa mayeso ake a giredi 7 caka catha.
C Yosefe anakonza bwino mu mayeso ake giredi 7 caka catha.
D Yosefe anapanga munshe mu mayeso ake a giredi 7 caka catha.

**ZOPUMIRA**

**Malangizo**

M'cigawo ici, funso liri lonse liri ndi ciganizo comwe sicinaikidwe zopumira. M'malo onse amene mufunika zopumirazi mwaikidwa manambala. Munsi mwa ciganizo ciri conse mudzapezamo njira yosonyezera kaikidwe ka zopumira m'malo muli manambala muja.

**Citsanzo:**

Amai andipatsa mpeni (1) nkhwangwa (2) khasu ndi mpini (3) ndipita nazo kumunda (4)

| | 1 | 2 | 3 | 4 |
|---|---|---|---|---|
| **A** | ! | , | ; | . |
| **B** | , | ; | . | . |
| **C** | , | , | . | . |
| **D** | . | . | , | . |

Yankho '**C**' ndilo loyenera.

Tsopano pakuyankha funso papepala lanu lamayankho, phimbani mkabokosi momwe muli lembo 'C' motere.

[ A ] [ B ] [ ] [ D ]

**Tsopano yankhani mafunso otsatira:**

**18** Kalanga ine (1) nkhuku yanga yagwidwa ndi bvumbwe (2) dzulo inanso inagwidwa m'mawa (3) Kodi nditani nazo nkhuku izi (4).

| | 1 | 2 | 3 | 4 |
|---|---|---|---|---|
| **A** | ? | . | . | ! |
| **B** | ! | . | . | ? |
| **C** | ? | , | , | . |
| **D** | ! | , | ? | ? |

**19** Tamusani anapita kukagwira nchito yowetera ng'ombe ku Chipata (1) tsiku lina ng'ombezo zinamuthawa (2) ha (3) zinaonongadi kabici m'dimba la Yelesani (4)

| | 1 | 2 | 3 | 4 |
|---|---|---|---|---|
| **A** | , | . | ? | , |
| **B** | . | , | ? | . |
| **C** | , | . | , | . |
| **D** | . | . | ! | . |

**20** Maiwase uziyankha akulu-akulu mwaulemu (1) kodi n'cifukwa ninji uyankha monyodola (2) tiye cokapo apa (3) ndidzakukwapula ukapitiriza (4)

| | **1** | **2** | **3** | **4** |
|---|---|---|---|---|
| **A** | ! | ? | . | . |
| **B** | . | ? | ! | . |
| **C** | . | ! | ! | . |
| **D** | . | . | ! | , |

## CIGAWO CACITATU

### Malangizo

M'cigawo ici, funso liri lonse liri ndi mau kapena ziganizo zinai zimene ziri ndi manambala osaikidwa mu m'ndandanda wa bwino. Ikani ziganizo izi mu m'ndandanda wa dongosolo la bwino kuti zonenedwa zonse zikhale zomveka bwino.

Werengani ziganizo zonse mosamala ndi kusankha njira yolongosoka potsatira manambala kuti zikhale mudongosolo lomveka bwino.

**Citsanzo 1:**

1 akonda
2 ambiri
3 sukulu
4 ana

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **A** | 2 | 1 | 3 | 4 |
| **B** | 4 | 1 | 2 | 3 |
| **C** | 4 | 2 | 1 | 3 |
| **D** | 4 | 1 | 3 | 2 |

Yankho **"C"** ndilo lolongosoka mu m'ndandanda. Nkhani yonse iyenera kukhala tere:

| A | B | | D |
|---|---|---|---|

4 ana
2 ambiri
1 akonda
3 sukulu

**Citsanzo 2:**

1 kodi ndiwe munthu wa mtundu wanji
2 sitidzayenda nawenso kuyambira lero
3 wosafuna kudzisamalira
4 umangoticititsa manyazi pa gulu la atsikana

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **A** | 4 | 3 | 1 | 2 |
| **B** | 3 | 2 | 4 | 1 |
| **C** | 1 | 3 | 4 | 2 |
| **D** | 2 | 4 | 3 | 1 |

Yankho "**C**" ndilo lolongosoka mu m'ndandanda. Nkhani yonse iyenera kukhala tere:

[ **A** ] [ **B** ] [ ] [ **D** ]

1 kodi ndiwe munthu wa mtundu wanji
3 wosafuna kudzisamalira
4 umangoticititsa manyazi pa gulu la atsikana
2 sitidzayenda nawenso kuyambira lero

**Tsopano yankhani mafunso awa:**

**21** 1 awiri
2 cimanga
3 muwambale
4 matadza

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **A** | 3 | 1 | 2 | 4 |
| **B** | 4 | 3 | 2 | 1 |
| **C** | 2 | 4 | 1 | 3 |
| **D** | 3 | 2 | 4 | 1 |

**22** 1 nsima
2 ali
3 anyamata
4 kudya

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **A** | 4 | 1 | 3 | 2 |
| **B** | 3 | 2 | 4 | 1 |
| **C** | 1 | 4 | 2 | 3 |
| **D** | 2 | 3 | 1 | 4 |

**23** 1 Cifukwa ca unyinji wa ziweto, Zandonda anaganiza zocoka pa mudzi.
2 Pa mudzi pa Chabwera, panali bambo wina dzina lake Zandonda.
3 Zina mwa ziwetozi zinali ngómbe, nkhumba, ndi mbuzi.
4 Zandonda anali ndi ziweto zambiri pa mudzi paja.

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **A** | 2 | 4 | 3 | 1 |
| **B** | 3 | 1 | 2 | 4 |
| **C** | 3 | 2 | 4 | 1 |
| **D** | 2 | 3 | 4 | 1 |

**24** 1 Kalilombe ndi Bechani anali ana omwe analephera mayeso a Giredi 7.
2 Patapita masiku khumi, anapita ku majiga ku kakwera basi.
3 Atafika ku Lusaka anapita ku nyumba kwa akulu ao.
4 Anyamata awiriwa anaganiza zopita ku Lusaka kuti akafune nchito.

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **A** | 4 | 3 | 2 | 1 |
| **B** | 3 | 2 | 1 | 4 |
| **C** | 1 | 4 | 2 | 3 |
| **D** | 2 | 1 | 4 | 3 |

**25** 1 Madzulo kutada, ana aja anauza makolo ao zimene anaona tsikulo.
2 Tsiku lina ana awiri a ngoma anapita kukasewera ku mtsinje.
3 Koma pamene ai ngoma atamva za nkhaniyo anacenjeza ana ake kuti asakapitekonso ku mtsinje kuja cifukwa mdani wao mkango ungawadye.
4 Kumeneko ana aja anakumanako ndi ana awirinso a mkango.

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **A** | 4 | 2 | 1 | 3 |
| **B** | 2 | 4 | 1 | 3 |
| **C** | 1 | 3 | 4 | 2 |
| **D** | 2 | 3 | 4 | 1 |

## CIGAWO CACINAI

### Malangizo

M'cigawo ici, mudzayesedwa ngati mungathe kudziwa matanthauzo a mau, madera a ziganizo kapena ziganizo zomwe. Munsi mwafunso liri lonse muli mayankho anai. Yankho limodzi cabe ndilo lopambana ena onse. Phimbani yankho mwasankha monga mwasonyezedwa pansipa.

**Citsanzo:** Tikati Belita **wapsa mtima** ndiko kuti ...
**A** anatentha mtima.
**B** mtima wake unali pamoto.
**C** mtima wake unapsa ndi moto.
**D** wakalipa kwambiri.

**Yankho "D"** ndilo loyenera.

[A] [B] [C] [ ]

**Tsopano yankhani mafunso awa:**

26 Mwambi woti '**Mako ndi mako usamuone kucepa mwendo**' utanthauza kuti ana ...
- A ayenera kulangidwa ndi makolo.
- B ayenera kumvera makolo.
- C ayenera kutamanda akulu-akulu.
- D sayenera kumvera makolo.

27 Andereya anakana mlandu kwa mutu wa galu. Tikati '**anakana kwa mutu wa galu**' titanthauza ...
- A kukana modandaula.
- B kukana monyoza.
- C kukweza mau pokana.
- D kukana molimba.

28 Tikati '**cala siciloza mwini**' titanthauza ...
- A kunena za mwini.
- B kupha ndi mankhwala.
- C kusadziweruza wekha.
- D cala sicilata mwini.

29 Kodi liu lakuti '**kulakwitsa**' titanthauzanji?
- A Kuwerengetsa
- B Kupumitsa
- C Kuganizitsa
- D Kucimwitsa

30 Mtolankhani wa ZNBC wanena kuti mliri wa Kolera wakhala wobvutitsa ku mzinda wa Kabwe. Liu lakuti '**mliri**' litanthauza ...
- A bvuto.
- B mantha.
- C nthenda.
- D zoopsa.

31 Liu la kuti '**nyengo**' litanthauza ...
- A nthano.
- B nthawi.
- C nyanga.
- D nyonga.

32 Amfumu anati, "**ulenje umasimba wako.**" Pamenepa atanthauza kuti ... wina.
- A osaulula cisinsi ca
- B osaba zinthu za
- C osabwereka ndalama za
- D tisamapempha-pempha khasu la

**33** Sofia anali wa zilubwe-lubwe. Tikati **wazilubwe-lubwe** ndiko kunena kuti wazikambidwe ...

**A** za pa mphala.
**B** za anthu wamba.
**C** zosafunsika n'konse.
**D** zosamveka bwino.

**34** Amai ... mawa kucokera ku Chipata.

**A** adzabwera
**B** adzawera
**C** azabwela
**D** azabwera

**35** Ngati munthu acita zinthu **zosakomera anzake** ndiye kuti wacita ...

**A** zabwino.
**B** zokondweretsa.
**C** za yekha.
**D** zosayenera.

**CIGAWO CACISANU**

**MALANGIZO**

Munsimu muli mau ndi ziganizo zolembedwa m'Cingerezi, sankhani yankho limene liri ndi liu kapena ciganizo cimene catembenuzidwa m'Cinyanja comveka bwino, mwa ziganizo zinai zapatsidwazo.

**Citsanzo:**

Tikati, **Belita is a polite girl**, m'Cingerezi ndi ... m'Cinyanja.

**A** Belita ndi mtsikana waulemu.
**B** Belita waulemu ndi mtsikana.
**C** ndi waulemu Belita mtsikana.
**D** waulemu ndi mtsikana Belita

**Yankho: 'A'** ndilo loyenera

**36** Liu lakuti, **elephant** m'Cingerezi ndi ... m'Cinyanja.

**A** Ngulube
**B** Ng'ona
**C** Njati
**D** Njobvu

**37** Liu la kuti; **chair** m'Cingerezi ndi ... m'Cinyanja.

**A** Gome
**B** Kama
**C** Mpando
**D** Situli

38 Ciganizo cakuti, **Corruption is not good** m'Cingerezi ndi ciphuphu ... m'Cinyanja.

A cipundula.

B ndi cabwino.

C ndi coononga.

D sicabwino.

39 Ciganizo cakuti, **Mahongo came yesterday** m'Cigerezi ndi Mahongo ... m'Cinyanja

A abwera dzulo.

B adzabwera dzulo.

C anabwera dzulo.

D wabwera dzulo.

40 Ciganizo cakuti, **Betty is a beautiful girl** m'Cingerezi ndi Betty ... m'Cinyanja.

A mtsikana ndi wokongola.

B ndi mtsikana wokongola.

C ndi wokongola mtsikana.

D wokongola ndi mtsikana.

**CIGAWO CACISANU NDI CIMODZI**

**Werengani nkhani iyi ndipo muyankhe mafunso otsatira.**

**Nkhani 1**

Mkhalidwe wonzunza ana wazika mizu makono. Ana ambiri-mbiri akhala yempha-yempha cifukwa ca mkhalidwe woipitsitsayu.

Kunzunza ana ndi bvuto lalikulu lomwe likhudza ana maka-maka aja amene makolo ao anabwira dothi. Nthawi zambiri timaona anawo akutumidwa kukagulitsa zinthu monga zitumbuwa mu makhwalala. Iyi ndi nthawi imene anawo ayenera kukhala ku masukulu kulandira maphunziro limodzi ndi anzao ena.

Masiku ena anawo amakumana ndi tsoka pamene akugulitsa malondawo. Mwacitsanzo, nthawi ya usiku anawo maka-maka ana akazi amagwiridwa ndi anyamata akulu-akulu ndikucita nawo za dama. Mwatsoka lanji amatengera matenda kapena pathupi posadziwika mwini.

Nthawi zina anawo, amaberedwera malonda ao. Kotero owasunga aja samacilandira ici. Zikatero ayamba kuwamenya ndikuwamana zakudya anawo.

Cifukwa ca zobvutazi, makolo conde tiyeni tionetsetse kuti tilabadira ana amasiye. Tisamawanzunza cifukwa cakuti alibe makolo ao polingalira mwambi uja wakuti, 'imfa ilibe odi.'

**Tsopano yankhani mafunso yotsatira awa (41 – 50).**

41 Ciganizo cakuti, **'akhala yempha-yempha'** citanthauza ...
- **A** kubvina-bvina.
- **B** kukondwa.
- **C** kukhumudwa.
- **D** kupempha-pempha.

42 Liu loti **'makhwalala'** litanthauza ...
- **A** makolo.
- **B** malonda.
- **C** mumiseu.
- **D** usiku.

43 Tikati, **'makolo ao anawasiya'** titanthauza ...
- **A** anakumana.
- **B** anamwalira.
- **C** anawamana.
- **D** sadziwika.

44 Ciganizo cakuti **'kunzunza ana'** Citanthauza ...
- **A** kukamba nao.
- **B** kusamalira ana.
- **C** kusautsa ana.
- **D** kutuma ana.

45 Ndi nthawi yotani yomwe ana amasiye amatumidwa kukagulitsa zitumbuwa?
- **A** Akacoka ku sukulu.
- **B** Nthawi ya sukulu.
- **C** Pa cuti.
- **D** Pakakhala alendo.

46 Ciganizo cakuti, **'tilabadira anawa'** citanthauza...
- **A** kukamba nao.
- **B** kuwasamalira.
- **C** kusathandiza.
- **D** kuwanzunza.

47 Kodi ndi tsoka lanji lomwe ana amasiye amakomana nalo? Ku ...
- **A** bvumbwidwa.
- **B** kugundidwa.
- **C** kutenga pathupi.
- **D** mangidwa.

48 Ciganizo cakuti, **'owasunga aja samacilandira ici'** Citanthauza ku ...

- **A** bvomerezedwa.
- **B** labadira.
- **C** menyedwa.
- **D** sabvomereza.

49 Sankhani mutu woyenera wa nkhani imene mwawerengayi.

- **A** Kugulitsa zitumbuwa kwa ana.
- **B** Kunzunzika kwa ana amasiye.
- **C** Kusowa makolo kwa ana.
- **D** Malonda ya ana amasiye.

50 Kodi ndi phunziro lotani limene tingatengemo munkhani imene mwawerengayi? ... ana amasiye.

- **A** Kusasautsa
- **B** Nchito
- **C** Osautsa
- **D** Zogulitsa

**Mayeso anu atha!**